# WHAT IS ISLAM?

## CHICHEWA TRANSLATION

# *KODI CHISLAMU NDI CHIYANI?*

## *(MALAWI)*

TRANSLATED BY:
HASIMI ISSAH | HASHIMIISSAHS@GMAIL.COM
Ali Issah | +27 65 721 3210



ABU ZAYD INSTITUTE

THEABUZAYDINSTITUTE@GMAIL.COM | +27 61 625 6070

## Zomwe zili Mkatimu


| | | |
|---|---|---|
| 1. | CHIYAMBI | II-IV |
| 2. | CHISILAMU NDI CHIYANI | 1-2 |
| 3. | NSANAMILA 5 ZA CHISILAMU | 3-14 |
| 4. | CHIFUKWA CHANI TINALENGEDWA KOMANSO MBIRI YA KUPEZEKA KWATHU? | 15-16 |
| 5. | MACHIMO AKULUAKULU MUCHISILAMU | 17 |
| 6. | CHIKHULUPIRIRO CHANU PA CHISILAMU | 18 |
| 7. | KUKANA ZIKHULUPIRIRO ZANU | 19-28 |
| 8. | UMBONI WA QUR'AAN | 29-36 |
| 9. | POMALIZA | 37-38 |

## 1) CHIYAMBI

MATAMANDO ONSE NDI A ALLAH, NDI ULEMU KWA MNENERI WATHU MUHAMMAD (MTENDELE UKHALE PA IYE).

Cholinga cha buku limeneli ndikuphunzitsa amene akufuna kudziwa zambiri zokhudza Chisilamu komanso kwa iwo omwe akufuna kumvetsa mwachidule za chisilamu. Kapena kwa amene avomereza Chisilamu Kukhala chipembedzo chawo koma sakudziwa zina zimene Chisilamu chimafunikira.

### *A. Kwa iwo omwe akufuna kudziwa zambiri za Chisilamu:*

Mulole kuti mutsogoleredwe panjira yowongoka. Mvetsetsani kuti umenewuso ndi mdalitso wa Mulungu (God). Tsiku lina Mkazi wina wantchito ankupemphera m'mawa kwambiri. Ali Mkati mopemphera, bwana wake anamumva mugowelo lake akupemphera, kuti *"Chifukwa cha chikondi chimene muli nacho kwa ine,(Mulungu)."* Nthawi yomweyo, bwana uja anamuletsa ndikumuuzanso kuti anene:

*"Chifukwa cha chikondi changa kwa inu, Allah (Mulungu)," osati:*

*"Chifukwa cha chikondi chanu kwa ine."*

Chimene bwana wake ankatanthauza ndi chakuti, monga ochimwa, mkaziyo sangathe kunena kuti Allah (Mulungu) amakonda iye. Koma mkaziyo mwamsangala anayankha kuti: "*Popanda Chikondi chake Allah (Mulungu) kwa ine, sindikanapatsidwa mphamvu zopemphera kwa Iye."* Mvetsetsani bwino kuti palibe chomwe chilipo, kapena chikuchitika, kapena chimachitika popanda chifuniro cha Allah (Mulungu). Ndiye, inuyo, Mukamawerenga bukuli, kaya cholinga chanu ndi kuphunzira zambiri zokhudza Chisilamu, kapena mukuphunzila chabe kufuna kukhala ndimaphunzilo apamwamba, kufuna kupeza zolakwika mu Chisilamu, kapena cholinga china chilichonse, ziwerenga bukuli monga momwe Allah (Mulungu) mwiniwakeyo akunenera. Ziwani mukuwerenga zinthu zomwe anthu ambiri sadzapeza mwayi kuti aziwerenge, ndichifukwa cha chilolezo cha Allah (Mulungu). Izi ndi zoona. Tsopano mutha kuganizirapo pa zomwe mwamvetsetsa ndikutsogozedwa moyenera.

Allah (Mulungu) akudalitseni, komanso olemba bukuli. Aameeni.

## *B. <u>Kwa iwo omwe alandira Chisilamu:</u>*

Takulandilani ku chipembedzo cha mtendere, M'bale/Mulongo wanga. Tikhalebe panjira yachiwongoko, njira ya anthu oyendetsedwa mowongoka osati Munjira ya anthu otayika. Mneneri Muhammad (mtendere uzikhala naye) ananena kuti aliyense amene alandira Chisilamu, amachotsedwa machimo onse amene anachita kale, ndipo

amakhala ngati mwana wankhanda yemwe alibe tchimo lililonse (oyera).

Ziribe kanthu zomwe mwakhala mukuchimwa kale, zonsezo zimachotsedwa mukalowa Chisilamu. Kodi Ambuye wanu ndi wachifundo motani?

Bukuli lifotokoza mwachidule mbali zazikulu za Chisilamu.

Anthu ambiri, kuphatikizapo anzathu ndi omwe timakhala nawo pafupi,

Amakhala ndi chidwi chofuna kudziwa tanthauzo lenileni la Chisilamu.

Koma atolankhani, kudzera mu upandu ndi ziphunzitso zosiyanasiyana, asokoneza tanthauzo lenileni la Chisilamu ndikulowetsa maganizo olakwika m'mitima ya anthu ambiri pankhani imeneyi.

Pachifukwa ichi, tikukhulupirira, ngati Mulungu (Allah) afuna, bukuli likupatsani Kuzindikira ndikumvetsa choyambirira chokhudza tanthauzo la Chisilamu.

## 2) **CHISILAMU NDI CHIYANI?**

Mawu oti Chisilamu amatanthauza **"Mtendere" ndi "Kudzipereka".**

### ***2.1. Mtendere:***

Chisilamu ndi chipembedzo chomwe chimalimbikitsa kukhazikitsa mtendere pakati pa zolengedwa za Allah (Mulungu), kaya anthu kapena ayi. Moni pakati pa Asilamu awiri, omwe ambiri amamva, **"Assalaamu Alaikum"** limatanthauza kuti *"Mtendere ukhale ndi inu."* Chisilamu sichimalimbikitsa nkhondo kapena kupha anthu osalakwa. Atolankhani asokoneza anthu ndi zolemba zomwe zimanamizira kuti Chisilamu ndi chipembedzo cha uchigawenga. "*Anthu okupha ndi mabomba*" ndi "*Azigawenga*" ndi mawu omwe atolankhani amawagwiritsira ntchito polumikiza Chisilamu ndi zochita zoyipa. Koma munthu aliyense amene ali ndi chidwi adzatha kuzindikira kuti:

**Sitiyenera kudalira kwambiri zomwe timamva kuchokera kwa atolankhani**.

Atolankhani ambiri samanena zoona ndipo nthawi zambiri amatsogolera malingaliro a anthu powona kuti izo mzomwe anthu amafuna kumva ndi cholinga chawo chozikidwa pa tsankho. Zintthu ngati zomwezi timaziona ngakhalenso mundare: kuti chifukwa chongomva nkhani yoti wakupha ndi

Msilamu (**amakhulupirira Chisilamu**), sizikutanthauza kuti ndi zoona. Ndikupusa kukhulupirira chilichonse chomwe timamva kapena kuwerenga kwa atolankhani.

Chofunika kwambiri kudziwa mchoti, ngakhale ngati munthu malo ena ake wachita "*Zauchigawenga*" ndi Msilamu, **izo sizitanthauza kuti munthu wina pamene wachita tchimo ndiye kuti chipembedzocho chikulimbikitsa kutero.** Izi zilingati ngati kunena kuti Hinduism imavomereza kugwirira anthu ena chifukwa munthu mmodzi wa Chihindu wachita chigololo kapena kuti Hinduism imathandiza chigololo chifukwa amuna ambiri a Chihindu amachita chigololo. Izi zikanakhala zopusa kwambiri.

### 2.2. ***Kudzipereka:***

Chachiwiri, Chisilamu Chimatatathauza kuti: kudzipereka kwa Allah (Mulungu). Kudzipereka kwa Allah (Mulungu) kumatanthauza kumlambira Mulungu yekha, ndikuzindikira kuti chiyambi cha moyo wanu chiyenera kukhala choperekedwa kwathunthu kwa Allah (Mulungu) yekha. Kudzipereka kwa Allah (Mulungu) kumatanthauza kusiya zonse zomwe Mulungu waletsa ndikuchita zomwe Mulungu walamula kuti muchite.

## 3) <u>SANAMILA 5 ZA CHISILAMU</u>

Mtumiku Muhammad (Madalitso ndi mtende zikhale pa iye) ananena kuti Chisilamu chamangidwa ndi sanamila 5. Tikambirana za sanamila zonse pansipa mura omodzi omodzi Payokha

### ***3.1.*** *SANAMILA YOYAMBA: Chikhulupiriro (Imaan)*

Imaan ndi chikhulupiliro. Ndi kukhulupirira, ndi mtima wonse, zinthu zofunika kwambiri za Chisilamu. Kuphatiizirapo izi:

#### ***3.1.1.*** Kukhulupirira Mulungu mmodzi yekha (Allah)

Monga Asilamu, timakhulupirira:

- Allah (Mulungu) ndi M'MODZI yekha.
- Allah (Mulungu) ndi wamuyaya.
- Allah (Mulungu) sanalengedwe, ndipo alibe ana.
- Allah (Mulungu) ndi wapadera. Palibe wofanana naye.
- Allah (Mulungu) si munthu.
- Allah (Mulungu) ndi wamphamvu kwambiri.
- Palibe munthu amene angathe kuchita chilichonse popanda ulamuliro wa Allah (Mulungu).

Mosiyana ndi ma Hindus, Asilamu amakhulupirira kuti kuli Mulungu M'MODZI yekha (Allah), osati ambiri.

Mosiyana ndi Akhristu, Asilamu amakhulupirira kuti Yesu (mtendere ukhale pa iye) SI Mulungu (Allah), koma mneneri wa Mulungu (Allah), monga Abulahamu, Nowa, Mose, ndi ena.

### ***3.1.2.*** <u>*Kukhulupirira mwa Angelo*</u>

Monga Akhristu, Ayuda, ndi zipembedzo zina, Asilamu nawonso amakhulupirira Angelo. Asilamu amakhulupirira kuti Angelo, mosiyana ndi anthu, alibe chilema (ndi angwiro komanso alibe tchimo). Iwo amapembedza Mulungu (Allah) nthawi zonse, ndipo ena mwa Angelo amaikidwa ndi maudindo ndi ntchito zawo zapadera zomwe amagwira.

Pali Angelo omwe ali ndi udindo woyang'anira za nyengo, ena omwe anasakhidwa kugwira ntchito yotenga moyo (imfa), ndipo wotchuka kwambiri pakati pa zipembedzo monga Chikhristu ndi Chiyuda ndi mngelo Jibraeel (yemwe amatchedwa Gabriel m’Chingerezi). Jibraeel ndi Mngelo amene ali ndi udindo wobweretsa chivumbulutso kwa aneneri osankhidwa ndi Mulungu (Allah). Komabe, tiyenera kuzindikira kuti ngakhale Angeloawa ali ndi maudindo amenewa, sangathe kuchita ntchito zawo popanda lamulo ndi mphamvu za Mulungu (Allah).

### ***3.1.3.*** Kukhulupilira M’mabuku omwe anavumbulutsidwa

M'Chisilamu, Asilamu amakhulupirira m'mabuku oyambirira omwe adaperekedwa kwa aneneri:

- Torati yomwe idapatsidwa kwa Moses (Musa).
- Masalmo omwe adapatsidwa kwa Davide (Dawood).
- Baibulo yomwe idapatsidwa kwa Yesu (Isa).
- Qur'an yomwe idapatsidwa kwa Muhammed (mulungu amdalitse).

Monga Asilamu, timakhulupirira m'mabuku onse oyambirira. Komabe, timakhulupirira kuti panthawi ya mneneri aliyense, buku la nthawi imeneyo lokha ndi lomwe linali lofunika kutsatira. Tsopano, m'nthawi ino, ndi nthawi ya Mneneri Muhammed (mulungu amdalitse) ndiye kuti titsate Qur'an, osati buku lina lililonse, Qur’an ndi lomwe liyenera kutsatiridwa.

**ZINDIKIRANI IZI**

- **Ayuda** amakhulupirira Mose (mtendere ukhale pa iye) ndi buku la (Torah) limene linavumbulutsidwa kwa iye, ndipo amakhulupirira kuti Davide sanapatsidwe buku lililonse, koma kuti anali munthu wolungama. Iwo amamukana Yesu (mtendere ukhale pa iye) ndi Muhammad (mtendere ukhale pa iye) ngati aneneri,

ndipo amati iwo anali onama. Amakhulupirira kuti Yesu (mtendere ukhale pa iye) ndi Muhammad (mtendere ukhale pa iye) analemba mabuku amene amati anavumbulutsidwa kwa iwo, ndipo kuti Mulungu mwiniwake sanavumbulutse mabukuwo.

- **Akhristu** amakhulupirira Yesu (mtendere ukhale pa iye) ndi buku la (Baibulo) limene linavumbulutsidwa kwa iye. Iwo amakhulupiriranso Mose (mtendere ukhale pa iye) ndi aneneri am'mbuyomu, ndipo amakhulupirira kuti Baibulo ndi buku la tsopano la Chiwongoko, lomwe lalowa mmalo mwa mabuku am'mbuyomu amene anavumbulutsidwa. Iwo amamukana Muhammad (mtendere ukhale pa iye) ndipo amati iye analemba Qur'an. Choncho, amakhulupirira kuti iye anali wonama, amene mwachinyengo ananena kuti Qur'an inavumbulutsidwa ndi Allah, pomwe anali iye amene analemba bukulo.

- **Asilamu** amakhulupirira buku limene linavumbulutsidwa kwa Mneneri Muhammad (mtendere ukhale pa iye) monga buku la chiwongoko (Qur'an). Amakhulupiriranso Yesu (mtendere ukhale pa iye) ndi Mose (mtendere ukhale pa iye), komanso aneneri am'mbuyomu. Komabe, amakhulupirira kuti mtundu uliwonse unkapatsidwa mneneri woti awatsogolere, ndipo m'nthawi ino, yomwe idzakhalapo mpaka tsiku la

chiweruzo, anthu ayenera kutsatira Qur'an yokha kuti apulumuke.

Mwachitsanzo, ngati munthu akanakhala ndi moyo m'nthawi ya Yesu (mtendere ukhale pa iye), buku la chiwongoko linali Baibulo, ndipo amene ankatsatira Baibulo anali pa njira yolondola. Koma amene sankatsatira anali osocheretsedwa. Koma m'nthawi yamasiku ano, yomwe ndi nthawi ya Mneneri Muhammad (mtendere ukhale pa iye), munthu ayenera kutsatira Qur'an kuti akhale wopambana.

### ***3.1.4.*** Kukhulupirira Aneneri

Asilamu, monga Akhristu ndi Ayuda, amakhulupirira kuti Mulungu (Allah) anasankha Aneneri pakati pa magulu osiyanasiyana a anthu kuti akhale ndi udindo woyitanila anthu ku njira yowongoka. Aneneri amenewa anapatsidwa udindo wachenjeza anthu kuti asachite tchimo, komanso kuwathandiza kuchita zinthu zabwino. Aneneri otchuka omwe anthu ambiri amawadziwa ndi awa: Ebrahim (Abraham); Nooh (Noah); Ismail (Ishmael) ndi ena.

Monga tanenera pamwambapa, Ayuda amakhulupirira Mose (mtendere ukhale pa iye) koma amakana Yesu (mtendere ukhale pa iye) ndi Muhammad (mtendere ukhale pa iye). Pomwe Akhristu amavomereza Mose (mtendere ukhale pa iye) ndipo amakhulupirira Yesu (mtendere ukhale pa iye)

koma amakana Muhammad (mtendere ukhale pa iye). Koma Asilamu amakhulupirira kuti onse awiri, Mose (mtendere ukhale pa iye) ndi Yesu (mtendere ukhale pa iye), anali aneneri, ndipo Muhammad (mtendere ukhale pa iye) ndiye anali mneneri wotsiriza ndi mapeto.

Kusiyana kwakukulu pakati pa Chikhristu ndi zipembedzo zina ndikoti Akhristu amakhulupirira kuti Yesu (mtendere ukhale pa iye) anali Mulungu (kapena mbali yake) osati munthu. Asilamu amakhulupirira kuti Yesu (mtendere ukhale pa iye) sanali Mulungu, koma mneneri basi.

Kodi n'zotheka kuti Allah (Mulungu) akhale munthu? Kodi si kupanda ulemu pa ulemerero ndi ukulu wa (Mulungu) ngati tingam'tsitse kufananiza ndi khalidwe la munthu? Kodi (Mulungu) angafune kugona, kudya, kapena kuchita zosowa zina zaumunthu monga momwe Yesu (mtendere ukhale pa iye) ankafunira? Kodi izi sizikutsitsa tanthauzo la Mulungu weniweni?

**ZINDIKIRANI IZI**:

Aneneri amasankhidwa ndi kutumidwa ndi (Mulungu) kuti atsogolere anthu. Iwo anali anthu wamba omwe ankakhala pakati pa anthu ena. Allah (Mulungu) anavumbutsila kuti akhale aneneri ake, powapatsa makhalidwe ofunika a uneneri. Mulungu anawapatsa udindowu pawa kumbulutso kudzera kwa mngelo Jibraeel (Gabriel).

## MUHAMMAD NDI NDANI?

Muhammad (mtendere ukhale pa iye) anabadwa mu zaka za m'ma 600 AD. Asanakhale mneneri, ankadziwika pakati pa anthu ake ngati munthu wachilunyamo ndi wolungama. Pa zaka 40, analandira chivumbulutso ndikupatsidwa ndime zoyambirira za Qur'an kudzera kwa mngelo Jibraeel (Gabriel) ndipo analandira udindo wa kukhala mneneri pakati pa anthu. Poyamba pa utumiki wake, ankanyozedwa ndi anthu. Komabe, kumapeto kwa moyo wake, chigawo chonse cha ***Arabian Peninsula*** chinatembenukira ku Chisilamu. Izi zinatheka mkati mwa zaka 23 zokha.

**ZINDIKIRANI:**
**ASANAKHALE MNENERI, MUHAMMAD (MTENDERE UKHALE PA IYE) SANALAMBIRE MAFANO KAPENA WINA ALIYENSE KUPATULA ALLAH (MULUNGU).**

### ***3.1.5.*** Kukhulupirira Kuuka kwa Akufa, Tsiku la Chiweruzo ndi Moyo Wotsatira.

Nsilamu amakhulupirira kuti dziko lapansi ndi lakanthawi kochepa ndipo moyo uliwonse udzalawa imfa. Pambuyo pake, tonse tidzasonkhanitsidwa pamaso pa Mulungu (Allah) pa tsiku lotchedwa Tsiku la Chiweruzo. Pa tsikuli, zochita zabwino ndi zoipa za munthu aliyense zidzayezedwa. Anthu omwe zochita zawo zabwino zimaposa zoipa adzalowa m'Paradaiso (Jannah), pamene omwe zoipa zawo zimaposa zabwino adzapita ku Gehena (Jahannam).

Kuphatikiza apo, anthu omwe anachita zolakwa zokhudza chikhulupiliro cha Islam adzalangidwa m'Gahena ngati atamwalira osalapa. Komabe, chifukwa cha chikhulupiliro chawo pa chisilamu, pamapeto pake adzaloledwa kulowa m'Paradaiso atamaliza kulandira chilango chawo.

Uku ndi kusiyana kwakukulu kwa Chikhristu, Akhristu Munjira yakaganizidwe kumbali yachitetezero (Yesu kufa pamtanda chifukwa cha machimo a anthu) amakhulupirira kuti Akhristu onse adzalowa m'paradaiso popanda kuweruzidwa.

Tiyerekeze kuti muli ndi ana 10. 9 mwa iwo ndi oipa kwambiri, ndipo wina ndi mwana womvera, wolungama. Tsopano tiyerekeze kuti mumakonda kwambiri mwana wolungama, ndipo mumakonda kwambiri iye, kodi mungaphe mwana wolungama ameneyu ndikunena kuti ana otsala 9 tsopano

akhoza kuchita chilichonse chomwe akufuna, kaya ndi kugwiririra ndi kupha, ndipo adzakhululukidwa chifukwa cha kuphedwa kwa mwana mmodzi wokondedwa wolungama uja? Kodi izi zingamveke?

Kupatula apo, Ndiye cholinga cha malamulo a uzimu ngati kuthandiza osowa, ndi kupewa machimo aakulu monga kupha/kugwirira, n’chiyani, ngati zili zoti m'moyo winawo aliyense adzalandira mwayi wolowa m’paradaiso, posatengera kuti atsatira malamulo kapena ayi?

Taganizani ngati mutasegula sukulu, ndipo ndinu mphunzitsi wamkulu. Kwa amene ali m’kalasi 1, nde ku kalasi mwaphunzitsa mwachizolowezi kuti chinthu chokhacho chomwe akuyenera kuloweza m’mayesero ndekuti 1+1 ndi = 2, kuti apambane bwino ndikupita ku kalasi 2. Tsopano yerekezerani ngati mwana wayankha yankho ngati 3, Kodi mwana ameneyu angakhale wakhoza bwino ndi kupita ku kalasi 2?

Uku ndikusiyana kwakulu pakati pachisilamu ndi chi Khristu, chifukwa chakuti Asilamu amakhulupilira Gahena ilipodi, ndipo kuti nawonso Asilamu akuyenela kukalowa ku Gahena ‘’kumoto’’ ngati akanike kutsatila malamulo Achisilmu.

**ZINDIKIRANI**: Chiwelengelo chawonetsa kuti anthu amene amakhulupirira kuti adzalowa kumtendere popanda kulangidwa ndi moto kugahena, amakhala ndi mwayi waukulu

wochita zoipa ngati kupha ndi kugwirira, chifukwa mwanjira ina iliyonse, amakhulupirira kuti adzalowa Kuntendere.

### ***3.2. SANAMILA YACHIWIRI: Pemphero (Salah)***

Kupemphera ndi chinthu chofunika kwambiri kwa Msilamu. Asilamu amapemphera **kasanu** patsiku. Choyamba amayamba kusanache m'bandakucha, chachiwiri nthawi ya masana, chachitatu pakati pa masana , chachinayi madzulo likangolowa dzuwa, ndipo chachisanu usiku.

### ***3.3. SANAMILA YACHITATU: Chopereka (Zakaat)***

Ngakhale chopereka chaulele kuchisilamu chimalimbikitsidwa kuchita, koma mawu oti *"Zakaat"* amatanthauza zopereka **zokakamizidwa** zomwe Asilamu ayenera Kupereka chaka chilichonse: **2.5% ya chuma** chawo chiyenera kulipidwa ngati zakaat.

Pali Asilamu ena omwe sakuyenelaa kupereka Zakaat chifukwa cha kuchepa kwa chuma chawo, ndalama ndizina. Zomwe zili zochepa kutengera ndi mulingo wa Zakaat. Zakaat imaperekedwa kwa Asilamu osauka omwe alibe chuma kapena zofunikira za moyo.

Cholinga cha Zakaat ndi **kupereka chifukwa cha chikondi cha Allah (Mulungu)**, komanso kuthandiza kuchepetsa mavuto amene anthu amakumana nawo. Kafukufuku

akusonyeza kuti aliyense padziko lapansi ngati atamalipira zakaat, padziko lapansi **sipangakhale umphawi**

### ***3.4. MSANAMILA YACHINAYI: Kusala (Swaum)***

Pafupifupi aliyense amadziwa tanthauzo la kusala. Koma mu Chisilamu, pa mwezi umodzi pachaka womwe umadziwika kuti **'Ramadhan'**, kusala n'kofunika kwa Asilamu.

Kuyambira nthawi ya m'banda kucha (pafupifupi mphindi 90 lisanatuluke dzuwa) mpaka kulowa kwa dzuwa madzulo,palibe chomwe munthu amene akusala akuyenela kudya.sikololedwa ngakhaleso kumwa madzi.

### ***3.5. Nsanamira Yachisanu: Ulendo opita ku (Hajj))***

Malo opatulika achisilamu ali m'mizinda ya Makka ndi Madina, Saudi Arabia.

Kaabah ili ku Makka. Asilamu amasonkhana mozungulira Kaabah ndikuchita tawaaf (mwambo woyendayenda ndi kupemphera mozungulira Kaabah kasanu ndi kawiri), ndi cholinga chopeza chikondi cha Allah (Mulungu).

Mzinda wa Madina uli pamtunda wa makilomita pafupifupi 500 kuchokera ku Makka, ndipo ndiwofunika kwambiri chifukwa Mzikiti wa Mtumiki Muhammad (mtendere ukhale pa iye) uli kumeneko. Ku Mzikitiwu kulinso manda a Mtumiki Muhammad (SAW) mwini wake.

Kamodzi pa chaka, pamakhala nthawi ya masiku 5 m'mwezi wotchedwa Zhul Hijjah (mu kalendala ya Chisilamu) imene Asilamu (omwe angakwanitse) amapita kukachita miyambo ya Haji m'madera opatulikawa (kosachepera kamodzi mu moyo wa munthu).

## 4) CHIFUKWA CHANI TINALENGEDWA KOMANSO MBIRI YA KUPEZEKA KWATHU?

Asilamu amakhulupirira kuti Allah (Mulungu), atamaliza kulenga dziko lapansi, adauza angelo kuti adzalenga anthu kuti akhale padziko lapansi monga mayesero a iwo. Anthu amene adzatsatire malamulo a Allah (Mulungu) adzapulumuka mkupita kumtendere komwe adzakhare muyaya, pomwe amene alephera kutsatira malamulo a Mulungu adzapita ku gahena (kumoto).

Angero adafotokoza nkhawa zawo pakulengedwa kwa munthu ponena kuti munthu sangatsatire malamulo a Allah (Mulungu) ndikuti iwo asalengedwe. Komabe, Allah(mulungu) adawauza angelo kuti "Ndithudi,ine ndikudziwa zokhuza munthu zimene inu simukudzidziwa”

Allah (Mulungu) adalenga Mneneri Adam kukhala munthu woyamba kulengedwa, ndipo adagwiritsa ntchito mdothi polenga Adamu, pomwe angelo adapangidwa kuchokera ku kuwala, ndipo ziwanda zidapangidwa kuchokera ku moto. Kenako Allah (Mulungu) adalamula Angelo kuti amugwadire Adamu pamaso pake pofuna kuonetsetsa kuti ukulu wa munthu ukukhazikika munthawi imene thupi lake linangomalizidwa kuumbidwa. Zonsezi zimachitikira kumwamba.

ZINDIKIRANI IZI: MA JINN ANALENGEDWA KUCHOKERA KU MOTO. ENA NDI ABWINO, ENA NDI OIPA. SATANA NDI

WA MKULU WA MAJINN. MU CHIISLAMU AMACHEDWA NDI IBLEES KOMANSO SHAYTAN.

Angelo anatsatira lamulo la Allah (Mulungu) ndipo anagwa kwa Adamu, koma Satana Mdyerekezi anakana kugwadadina chifukwa cha kunyada, ndipo ananena kuti anapangidwa ndi moto pamene anthu anapangidwa kuchokera ku dongo. Chotero, iye ananena kuti sikungakhale koyenera kugwadira chinthu chopangidwa kuchokera ku chinthu chochepa. Chifukwa chake, Allah (Mulungu) adatulutsa ma Ibles kuchokera kumwamba. Asanatulutsidwe, Iblees adamuuza Allah (Mulungu) kuti adzatsimikizira kutsika kwa munthu pomusokeretsa munthu kwa nthawi yonseyi.

Adam adadzimva kukhala yekhayekha m'paradiso, ndipo Allah (Mulungu) adalenga Hawa (Eva) kuti akhale bwenzi lake ku paradiso. Pambuyo pake, Allah (Mulungu) adawatumiza Adamu ndi Hava padziko lapansi kumene anthu adzakhalamo mpaka tsiku lachiweruzo. Adamu anapatsidwa malamulo ndi malangizo oti azitsatira, komanso kuti ana ake azitsatira.

Chifukwa chakukhalapo kwathu mophweka, ndikupembedza Allah (Mulungu). Dzikoli ndi mayeso ndipo ndi lanthawi yochepa. Kwa nthawi yochepa yomwe tili pano, tiyenera kulambira Allah (Mulungu) ndi kuchitira zolengedwa zake (anthu ndi nyama) mwachifundo ndi ulemu. Komanso, zimene timakhulupirira ziyenera kugwirizana ndi zimene tatchulazi.

## 5) **MACHIMO AKULUAKULU**

- Kumphatikiza Allah (Mulungu) ndi zinthu.
- Kunyalanyaza mapemphero 5 tsiku liliIonse.
- Kupha.
- Kulephera kupereka Zakaat popanda Chifukwa.
- Kulephera kusala kudya mu Ramadan popanda chifukwa chomveka.
- Kuchita matsenga akuda.
- Kulephera kuchita Haji ngati ali ndi njira.
- Kugonana musanalowe m'banja.
- Chigololo.
- Kulipiritsa ndi kulandira chiwongola dzanja.
- Kuthetsa ubale wabanja wa pantundu wanu.
- Kumwa mowa/zoledzeretsa.
- Kudya nkhumba ndi zowola.
- Kusalemekeza makolo.
- Kukhala mtsogoleri wosalungama.
- Kuchitira ena nkhanza.
- Kusaona mtima.
- Kumvetsera nyimbo.
- Kusinjirira ena.
- Kuba/umbava,

## 6) CHIKHULUPILIRO CHANU PACHISILAMU

Ngakhale simunayankhulepo momveka bwino, kapena simunaganizirepo,, koma ngati simukhulupirira chisilamu, zimatanthauza kuti mukukhulupirira kuti Mtumiki Muhammad (saw) ndi wabodza - kuti sanali Mtumiki (SAW) ndikutiso Qur’an idalembedwa ndi iye, ndipo siinavumbulutsidwe ndi Allah (Mulungu).

Palibe amene angavomereze kuti Qur'ani ndi mawu a Allah (Mulungu),pokhapo akhale akuvomereza Chisilamu. Monga momwe Qur'ani ikunenela kuti palibe njira ina, kupatula njira ya chisilamu, yomwe ndi njira yowonadi.

## 7) UMBONI WOTSUTSA CHIKHULUPILIRO CHANU

Pofuna kupangitsa kabukuka kachidule ,kutsutsa kotheratu kwa chipembedzo chilichonse/zikhulupiliro ziti kulibe Mulungu sitinayikemo.

Ife tikukhala ku Johannesburg,South Africa ,ambiri omwe timakumana nawo ndi omwe sali Asilamu Koma Akhristu.Pachifukwa ichi,Mtsutso wachidule koma omveka kwa uzachitikapo.

Ngati wowerengayo ndi wosakhulupirira kuti kuli Mulungu/kuti Mulungu alipo titumizireni mwachifundo kudzera pa imelo (zambiri zathu zatchulidwa pachikutopo)ndikupempha buku lathu “Disproving Atheism in 10 minutes “.

**ZOFUNIKA KUDZIWA**

Chisilamu simalimbikitsa kusalemekedzana ndi chidani. Chilichonse chokhudza kutsutsa zipembedzo zina chomwe chili m’bukuli cholinga chake ndikulangiza ndi kutsogolera anthu pa njira yoyenera,osati kunyoza kapena kuipitsa ena.

## a. KUTSUTSA CHIKHRISTU:

Chikhristu titha kuchigawa magulu awiri:

## 7.1. KWA AMENE AMAKHULUPIRIRA ZA UTATU WA MULUNGU

Akhristu ambiri amakhulupirira m'Kamvedwe kovutirapo ka utatu (Mulungu;yesu;Mzimu Woyera) .

Akafunsidwa, pafupifupi akhristu onse omwe ndalankhulana nawo ,samamvetsetsa momwe utatu umagwirira ntchito pofuna kumvetsetsa za izi.

NSANAMIRA ZA M'CHIKHULUPIRIRO CHAWO NAZI:

1) Yesu ndi Mulungu

2) Atate,Mwana (Yesu),ndi Mzimu woyera ali Olingana ndi Wosatha

Tiyakha n,kulingalira kwawo mosiyanitsa pansipa motere:

YESU NDI MULUNGU

- Molingana ndi chikhulupiriro chawo cha Utatu wa Mulungu,kotelo amati Yesu ndi Mulungutso. Atate,Mwana ndi Mzimu woyera mwachimodzi mwa

izo zikupanga 1/3 ya mukupezeka kwa chiyambi cha Mulungu:

- Ngati zili chonchi,tsopano bwanji pamene Yesu analamula ophunzira ake kuti apemphere,ndiyeno kenako anapemphera yekha mwa kugwada,**(mateyu 26:39)**,kodi anali kugwadira ndani?

- Kuonjezera apo,m’buku la **Mateyu (27:46),** khani ya kupachikidwa pa mtanda yalembedwa kuti Yesu (mtendere ukhale pa iye) akufuula kuti ”Eli,Eli,lama sabakatani”kunthandaudza kuti”Mulungu wanga,Mulungu wanga, mwandisiyilanji ine?” choyamba, ngati Yesu ndi Mulungu, akufuulira ndani?Chachiwiri, ngati alidi Mulungu, akulira kuti wadzisiya yekha?

- Ngati Yesu (mtendere ndimadalitso akhale pa iye) adali 1/3 ya mulungu, kodi tsono mulungu amagona ,kudya/ kupita ku chimbudzi ,kodi ameneyu tsono angakhale mulungu?

- Akhristu amakhulupirira kuti yesu (mtendere ndi madaritso akhale pa iye) adapachikidwa pa mtanda. kodi ndiye kuti 1/3 ya Mulungu idafa pa nthawi imeneyo ?

- Malingana ndi chikhulupiriro cha imodzi mu utatu .yesu ndi 1/3 ya mulungu, kunena kuti ndi mulungutso pa iye yekha ngati izi zili chonchi ndiye kuti yesu ndiwozindikira ndikuziwa zonse sichoncho?

  M'buku lochewa **(maliko 11,12-14)** zanenedwa kuti pamene yesu adava njala, adafuna kudya ,pamene amachoka ku Betaniya,yesu ananva njala Ataonera patali mtengo wamkuyu uli ndi masamba ,anapita kuti akaone ngati unali ndi chipatso chilichonse .Atafika ,sanapezemo kanthu koma masamba ,chifukwa sinali nthawi ya nkhuyu kenako iye adawuthembelera mtengowo ,umo ndimene m'buku la maliko lafotokozera.

  Nfuso kumati ngati iye yesu adali woziwa zonse ,monga alili Mulungu bwanji sadathe kudziwa zokhuza mtengowu (kuti sinthawi yake yobala zipatso ) kufikila atawuwona mtengowo muchiyembekezo chake .

- Ngati ukulu wa yesu (mtendere ukhale pa iye ukuchokera kwa iye kubadwa opanda bambo nsono m'chifukwa ninji akhristu samalambira adamu chifukwa chokhala opanda mayi ndi bambo?

## KULINGANA NDI KUSATHA KWA UTATU WA MULUNGU

Pali njira ziwiri zosonyeza mkhristu olakwika za chiphuzitso cha utatu woyera .Tifotokoza njira ziwirizi pansipa :

### NJIRA YOYAMBA :UMBONI WONGOGANIZA

Mu mipingo ya lamulungu ,mawu oti atate mwana ndi mzimu woyera amatchulidwa mobwerezabwereza m'matchalichi, chifukwa ichi ndi mfundo yaikulu ya chikhulupiriro chawo

Ngati zoonadi atate ,Mwana (yesu,)ndi Mzimu woyera ali olingana ndi wosatha ,mfunso likubwera ngati atate afuna kuti chivomelezi chichitike ,kodi atate amafuna chilolezo cha yesu (mtendere ukhale pa iye ) ndi mzimu woyera ?kodi apa pamakhala msokhano chisakho chilichonse chisanapangidwe ?

**NGATI INDE CHILOLEZO CHIMAFUNIKA**,izi zikanatanthauza kuti amakhulupirira kuti atate yemwe amayenera kukhala wodzilamulira payekha (monga khalidwe la mulungu ),amafunira chithandizo cha yesu (mtendere ukhale pa iye ) ndi Mzimu woyera .izi zikanatanthauza kuti allah (mulungu) ndi wodzilamulira Koma wodalira ena chifukwa chake ,izi so zomwe (nthawi zina zimatchedwa chinsinsi chopanda tanthauzo ).

Kodi zingamveke kuti allah (mulungu ) ndi mulungu amene

amafunikira chilolezo cha ena? Lingaliro la mulungu ndiloti iyeyo ndiye amene amafunikira chilolezo cha ena .

Ngati atate amafunikira chilolezo cha yesu (mtendere ukhale pa iye )ndiye kuti pamene yesu (mtendere ukhale pa iye )amati anakhomeredwa pamtanda, kodi yesu analetsa chisankhochi asanakhomeredwe?

Kumbali inayi ,**NGATI ZOSATHEKA KUFUNIKA CHILOLEZO**: pamenepa amatsutsa mfundo yayikulu ya chiphunzitso chawo ,choti aliyense amene ali mbali ya utatu ndi WOLINGANA NDI WOSATHA

Tangoganizani kuti pali bizinesi yoyendetsedwa ndi mabwenzi atatu omwe onse ali ndi magawo ofanana mumgwirizano .kodi bwenzi limodzi lingagulitse galimoto yamalonda popanda chilolezo cha ena ?Ayi .chifukwa onse ndi ofanana .

Mofanana momo ,mwachitsanzo ,mvula iyenera kugwa kuchokera kumwamba ,mwa mfundo ya wofanana ,atate adzafunika chilolezo cha Mwana kuti mvulayo igwe ,isanagwe ,apo ayi sangakhale wofanana .Koma ngati izi ndi zoona ,kodi izi zimapangitsa atate kukhala wodzilamulira payekha ?chimene chiyenera kukhala khalidwe la mulungu .

Kutsutsa kuli pamwambaku kungagwiritsidwe ntchito motsutsana ndi chihindu ,popeza lingaliro la milungu yambiri (milungu yoposa m’modzi )iri ndi chinyengo chofananaso

,kaya ndi njira ya milungu itatu (monga momwe zilili pamwambapo )kapena milungu 300 (chiwerengero chilichonse chomwe chinganenedwe ndi ahindu ) mzofanana

NJIRA YACHIWIRI :KUSOWA KWA UMBONI OTI ATATE, MWANA NDI MZIMU WOYERA NDI OFANANA NDI WOSATHA MU BAIBULO

Monga tanenela pamwambapa,kuti munthu akhale khristu akuyenela kukhulupirira kuti atate,mwana ndi mzimu ali wolingana ndi wosatha.Ngati simukhulupirira izi,ndiinu opanduka,otaika,siinunso m'khristu.

Komabe ngakhale zili chonchi ,chodetsa nkhawa kwambili n'choti ,mbaibulo lonse ,mulibe vesi lomveka bwino limene limanena kuti onse atatu (atate ,mwana ,ndi mzimu woyera )AKULINGANA NDI WOSATHA .

Ndithudi ,buku lopatulika liynera kunena momveka bwino komanso mopanda chikaiko za chikhulupiriro chachikulu cha chipembezo chimene likulalikira ,sichoncho ?

Taonani izi mosiyana ndi chisilamu ndi quran .chiphunzitso cha chisilamu ndi TAUHID (umodzi wa allah )osati milungu itatu monga imafalitsidwa mu chikhristu komabe ,chikhalidwe cha chisilamu chafotokozedwa momveka bwino mu quran, m'mutu 112 lotchedwa “mutu woona mtima “momwe Allah akunena kuti:

1.Nena kuti iye ndi mulungu m’modzi
2.Mulungu Ngwamuyaya
3.sabala kapena kubadwa
4.Ndipo palibe chofanana ndi iye

Chifukwa chake ,phunzitso lachisilamu limatchulidwa mosakayikira ,zomwe ziyenera kukhala choncho ngati bukhulo ndi laumulungu .liyenera kukhala bukhu lomveka bwino, osati kuyambitsa chisikonezo chochulukirapo, apo ayi ndiye kuti likuononga cholinga chomwe linavumbulutsidwa .

Apa zikuvuta kumveka bwino ndi kusatsimikidzika komwe chikhristu chikuyambila ndi kukhadzikitsidwa kwake,kuwunika mwachidule olo ndi mbili yakale mafokozedwe ake siziziwika momwe chikhristu chinayambila.

Pafupifupi zaka 300 pambuyo pa kupachikidwa kwa yesu pa mtanda ,munthu wina dzina lake constantine anakhala mfumu ya constantinople (masiku ano ,istanbul ,turkey) ndipo poyesera kupeza chithandizo ,analengeza kuti anategera chikhulupiriro chachikhristu .dongosolo lake linatheka kwambili ,popeza ufumu wake unakulanso kwambili, ndipo akhristu mwamsanga analumbira kupereka chithandizo chawo pa izi chifukwa cha kukhulipilika kwake komabe ,pasanapite nthawi yaitali ,iye anakumana ndi vuto mkati mwa izi.

M’modzi mwa akuluakulu oyambirira a mpingo ,arius ,anali ndi lingaliro lakuti atate anali wamkulu kuposa mwana ,yesu ndiye kuti sanali ofanana .pomwe kumbali ina kunali Athanasius ,yemwe anali bambo wa tchalitchi choyambirira amene ankhulupirira mfundo ya ofanana.

Chifundo chake, constantine ,pofuna kuthetsa mgwirizano womwe unkakulira ,womwe pamapeto pake ukanagawa ndi kufooketsa ufumu wake ,adaganiza zokonza msonkhano mu chaka cha 325AD ,womwe unadzakhala wotchuka ngati council of Nicaea .

am’sonkhanowu , mabishopu ochokera konsekonse adaitanidwa kuti avotere kapena kutsutsana kukhazikitsidwa kwa mfundoyi “ OFANANA NDI OFANANA NTHAWI ZONSE ‘’ndipo apa chifukwa ,mwachionekere ,panalibe umboni wotsimikizika wokhudzana ndi izi

Mwinamwake ,liwu lakuti “kuvota” lingakhale lolakwika popeza bishopu aliyense amene anatsutsa lingaliro loterolo anayang’anizana ndi chiwopsezo cha kuthamangitsidwa,ndipo anakakamiza kuvota mokomera .izi zikutsimikiziridwa momveka bwino kuti arius ,yemwe anali mtsogoleri wa chipani chotsutsa (chotchedwa Arius ) anakana kuvota mokomela maganizo oterowo ndipo pambuyo pake anathamangitsidwa .

Choncho maziko achikhulupiriro chawo ,kutathauza

kumvetsetsa kwa utatu wa Mulungu sikunatchulidwe kokha muchipangano chakale komanso palibe paliponse palembedwa muchipangano chatsopano!Ndiyeno kodi Allah(Mulungu)angafune kuti wina akhulupirire chithu chosafotokozedwa bwino?

**7.2. Amene amakhulupirira kuti Yesu(mtendere ukhale pa iye) sali Mulungu koma ndi m'neneri(m'neneri womaliza) ndi amene amakhupirira atate ndiwakulu kuposo mwana(m'neneri womaliza) koma sakhulupirira kuti Muhammad (madalitso ndi mtendere ukhale pa iye )ndi mtumiki wa mulungu .**

Izi zitha kutathauza kuti iwowa so akhristu Koma mulimonse momwe zingakhalire ,umboni wa izi udzakhala mu umboni wa Quran .aliyense amene atsatira chikhulupirirochi angafunire kutsutsa kulondola kwa Quran kapena kupeza chowiringula /chifukwa cha chozizwitsa chilichonse cha Quran.

## 8.) UMBONI WA QURAN

Umboni wa Qur'an ukhoza kukhala pa wiri. Choyamba, pomwe gulu lina lili ndi udindo wotsutsa Qur'an.Ndipo Chachiwiri, pomwe udindo Uli pa Msilamu kuti atsimikize Qur'an.Mosasamala kanthu kuti ndi njira iti yomwe ingatsatidwe, zisonyezo za Qur'an zidzawonekera, popeza Asilamu sakuyenera kupewa mtolo Wotero wa Umboni.

Njira zofuna kuyiyesera Qur'an zilipo zinthu zinayi zofunika Kwambiri

8.1. kumbali yakakhonze kazinthu

Qur'an pa yokha imatsutsa anthu.Quran ikutsutsa aliyense kuti atulutse sura IMODZI, Kapena gawo lake ndi kupikisana nayo ndi Qur'an **[mutu 2: vesi 23]**

Popeza kuti amene sali Asilamu amakhulupilura kuti Mtimiki Muhammad (SAW) adali wambodza chabe yemwe adayambitsa Qur'an, apa akuuzidwa kuti atulutse sura imodzi Kapena gawo lake lofanana ndi lomwe lili mu Qur'an.Qurani ikuwatsutsa onse kuti atsimikize zonena zawo.

Ngati ukhulupirira kuti Qur'an ndi mawu aAllah (Mulungu), ndiye kuti ndithu ndiwe Msilamu. Komabe, dziwani kuti Qur'an ikunena kuti Chisilamu chokha ndi chomwe chingatsatidwe. choncho simunganene kuti inde, ndi mawu a Allah (Mulungu) koma ine sindine Msilamu.izi zingakhale ngati kunena kuti munthu kuwerenga zala zanu kuti 1+1=2

koma mumatsatira chikhulupiriro chakuti 2-1=3.

## 8.2. KUMBALI YA CHITETEZO

**QURAN**

Mpaka pano, Quran ndi Malemba Okhawo Omwe adavumbulutsidwa, Omwe sadasinthe. Ichi ndi chowonadi chambiri chosatsutsika. Quran Yasungidwa Kudzera M'malemba Olembedwa Komanso M'mitima Ya anthu. Ana ang'onoang'ono, azaka 4 ndi zaka 5 adaloweza Quran Kuyambira Pachiyambi mpaka Kumapeto. Zomwe Zikutanthauza Kuti palibe mwayi Wosintha.

**TORAH**

Komabe, Torah, Yomwe idatumizidwa Kwa mose (mtendere ukhale pa iye) idasowa Kotheratu ndipo izi Zikutsimikiziridwa ndi chenicheni chakuti Pa nthawi Ya Yesu (mtendere ukhale Pa iye) Panali Matembenuzidwe Anayi Osiyanasiyana a Torah. Mowonjezela apo Torah (Yachipangano chakale) Zanenedwa kuti idasungidwa mu umfumu wa Yudasi m'nyumba Ya mulungu. Mbiri zikufotokoza kuti nyumba Ya mulungu ' imeneyo idagumulidwa kokwana Kawiri. Koyamba ndi mfumu Ya ku Egypt. Kachiwiri ndi mfumu ya ku Israel. Torah lidathela pamenepa Panalibe Chisimikizo chenicheni Choti bukuli lilipo. Zidasimikizidwa kuti lidawonongedwa. Chodabwitsa ndichoti patapita zaka 18 pambuyo pa Kulowa kwa umfumu wa mfumu Josiah. Mfumu Yapamwamba Yochedwa Hilkiah munjira ina idapeza Torah yi mu nyumba yomweyo Patadutsa zaka 18.zoti anthu akafukufuku ena

adakanika Kupeza Umboniwu **(mafumu 11 mutu 22 ndi Akatorika mutu 34)** Awa ndimaganizo Osatheka, malo mwake mwini Wake Hilkiah adayiwala Kulemba nkhaniyi Yoti adapezadi bukuli mu mbiri zake.

**BAIBULO**

Koma Baibulo la Yesu silitsutsidwa mosakayika kuti likupezeka masiku ano. M'malo mwake, Pali chipangano Chatsopano Chimene Chapangidwe ndi Mabuku Olembedwa ndi anthu monga mateyu, marko, Luka ndi Yohane. Chifukwa Chake, nthawi Zambiri Mumamva anthu akunena kuti "Buku la Mateyu". Kachiwirinso, ndi Mfundo Yosatsutsika, imene ingatsimikiridwe ndi Akatswiri achikristu Ophunzira kuti"Mabuku" amenewo sanali Ochokera Kwa Mulungu, Koma Olembedwa ndi anthu Otchedwa (mateyu, Marko, Luka ndi Yohane),amene akuti anali ophunzira a Yesu.komabe, mkangano wochirikiza chifukwa chake likuvomerezedwa kukhala Baibulo lamakono,ndilo chiphunzitso chakuti polemba mabuku amenewa,iwo (ie,Mateyu, Marko,Luka ndi Yohane)anathandizidwa ndi mzimu woyera, ndipo motero amawapanga mabuku awo ndi auzimu.

**ZINDIKIRANI: LUKA YOHANE, MARKO NDI MATEYO, AMENE UTHENGA WABWINO UMANENA KWAIWO,SANALI OPHUNZIRA A YESU! ANALI AKATSWIRI OMWE ANACHITIKA KUGAWANA DZINA LIMODZI NAWO! OPHUNZIRA KWAMBIRI ACHIKHIRISTU ALIBE UMBONI WOTI ACHITIRE ENA.**

## 8.3.Kumbali ya zotsutsana

Mpakana pano, palibe amene adanenapo kuti Qur'an ili ndi zotsutsana.Ngakhale tikukhala mum'badwo wofufuza nthawi yomweyo chifukwa cha intaneti , PALIBE munthu amene adapezapo zotsutsana mu Qur'an.M'mabuku ambiri, wolemba amayamba ndi kupepesa pazolakwa zili zonse zomwe adapanga m'bukuli. koma Qur'an yayamba NDI kunena kuti Qur'an ilibe cholakwa chilichonse. **[Qur'an:mutu 2:vesi 2]**

Simupeza malo amodzi a Qur'an kuti 1+1=2, pomwe kwina akuti 1+1=3.

kumbali ina,tikayang'na m'mabuku ophatikizidwa m'Baibulo, pali zolakwa zowonekera m'nkhani ya zochitika zina.

Nkhani yachikhristu yokhudza kupachikidwa kwa Yesu imati Yudasi ndiye wotsutsana ndi nkhaniyi. Munthu amene anaulula za Yesu, zomwe zinachititsa kuti apachikidwe pamtanda. Zogwirizana ndi mutu waung'ono uwu, ndi nkhani zosiyana za Yudasi wotsatira pambuyo pake.

**Bukhu la Mateyu (27:3-8)** limasonyeza kuti Yudasi anadzimvera chisoni pambuyo pa kupachikidwa kwake chotero,anataya ndalama za chiphuphu zimene analandira

Chifukwa choulula kumene yesu anali ndipo anadzipha pambuyo pake.

Pamene, **m'Buku la Machitidwe a Atumwi (1:18),** Yudasi akulembedwa kuti adagula munda ndi ndalama za chiphuphu, ndipo polowa m'mundamo, adaterereka nafa Chifukwa cha matumbo ake kutuluka.

Izi ndizotsutsana zoonekeratu, komanso kusiyana kwakukulu m'maakaunti operekedwa. Ngati olemba mabukuwo anathandizidwa ndi mzimu woyera, kodi wina wa Utatu akanalakwa popereka nkhani zosiyanasiyana za Yudasi kwa olemba awiri amene tawatchulawa?

Kodi buku lingavomerezedwe kukhala laumulungu limene liri ndi zotsutsana zomvekera bwino motero?

8.4. Kumbali ya zozizwitsa

### 8.4.1. Machilitso kapena zachipatala

Qur'an ikufotokoza momveka bwino magawo a kubadwa kwa munthu; kutchula gawo lililonse la kutenga pakati kwa munthu, ndiyeno kufotokozanso za mluza [mutu 27:vesi 12-14]. Kumapeto kwa zaka za m'ma 1800 ndi pomwe akatswiri azachipatala, kudzera muukadaulo, adakwanitsa kudziwa zomwe Qur'an idafotokoza pafupifupi zaka 1250 izi zisanachitike.

### 8.4.2. Maulosi

Munthawi yomwe ufumu wa Perisiya unali wamphamvu

kwambiri, Qur'an idaneneratu kuti Aroma adzagonjetsa Aperezi mkati mwa zaka 9 **[mutu 30: vesi 2-4].**

Ichi ndi chozizwa chomwe chikadapanda kuchitika, ndiye kuti nthawi yomweyo itsutsa Qur'an. Pakali pano, tingathe kuganiza zimene zinachitika pambuyo pake: Aroma anagonjetsa Aperis

Ichi ndi chozizwitsa chomwe munthu akagwiritsa ntchito malingaliro ake, chimakhala chodabwitsa. Nkosavuta kuchita mwai wamwayi n'kuuza munthu wapamsewu kuti tsiku lina adzalemera. Popeza kuti nthawi yake siidatchulidwe, ndiye kuti pali nthawi yokwanira yoti izi zichitike.

Kumbali ina, ngati mukuyenera kuuza munthu wina kumbali ya msewu kuti mkati mwa thawi yoikidwiratu, mwachitsanzo, zaka 9, mudzakhala wolemera kwambiri, pali zovuta zambiri zomwe zimawonjezeredwa, monga kulephera kukhala wolemera kumabweretsa kutsutsidwa kwa kuneneratu kwake, ndipo zonena za uneneri zidzathetsedwa m'menemo.

N'zodziwikiratu kuti Aroma anali ofooka kwambiri pa nthawi imene nkhaniyo inkanenedwa, zinali ngati kulosera kuti posachedwapa mwana wakhanda adzamenya msilikali wodziwa zambiri. Mowonjezela apo ma buku a mbiri zakale zalembeda kuti pakazapita zaka 8, ngakhale zimawoneka kuti zosatheka kuti Aroma angapambane pogonjetsa ma perisi. Posakhalitsa, mogwirizana ndi ulosi wa Qur'an mwachitsanzo, kupambana mkati mwa zaka 9, Aroma adapambana.

### 8.4.3. Sayansi

Qur'an imatchula nyumba ya kangaude kuti ndi" nyumba zochepetsetsa kwambiri" **[mutu 29: vesi 41].**

Akangaude aakazi ndi aamuna akathamangitsana ngati yaimuna siithawa msanga, yaikaz imadya yaimuna. Nthawi zambiri, nyumba imamangidwa kuti iteteze, pamene kwa akangaude, imamangidwa kuti iwononge omwe amalowamo. Ichi ndi chizizwitsa cha Qur'an.

Qur'an ikunenatso kuti kangaude wachikazi ndi amene ali ndi udindo wopanga nyumba. Sayasi tsopano ikutsimikizira kuti ndi kangaude wankazi amene ali wamphamvu pa ziwirizo **[mutu 29: vesi 41]**

Qur'an ili ndi zozizwa zambiri, zambiri zomwe sitingazitchule m'kabuku kakang'ono. Koma pamwambapa ndi zina mwa zozizwitsa zambiri zomwe wowerenga aliyense angaganizire.

Lingalirani izi. Kodi Pali aliyense amene anganene kuti zaka 1447 Zapitazo, Munthu amene, M'mbiri Yakale, amavomerezedwa Kukhala Wosakhoza kulemba buku laulemelero chotero?

Inu, monga Owerenga, mwapatsidwa Chidziwitso, m'malo Mochigwiritsa ntchito Kutsutsa, Kusinkhasinkha ndi Kulingalira.

MTUMIKI (Mtendere Ukhale PA IYE) ANANYOZEDWA CHIFUKWA ANATAYIKIRA ANA AKE AWIRI PAKATI PA UCHIMWANA WAWO. OSAKHULUPIRIRA AKATI ALI NGATI NYAMA YOPANDA MCHIRA I.E. CHOLOWA CHAKE CHIZATHA POPANDA MWANA WA DZINA LAKE. ANATHEMBEHELEDWA NDI MA AYA AMA QURAN KUTI OMWE AMUNYOZA MTUMIKI (Mtendere Ukhale Pa Iye) ADZAKHALA.

OTERO AYIWALIKA. NDIPO DZINA LA MNENERI (Mtendere Ukhale PA IYE) LIDZAKUMBUKIRIDWA KWA muyaya.

LERO, NDI ZOONA ZA PADZIKO LONSE, KUTI DZINA LO SAYIWALIKA KWAMBIRI NDI “MUHAMMAD”.

MUNTHU YEMWE AKASEKEDWA, KUNYOZEDWA NDI KUTUKANIDWA, M’KUPITA KWA NTHAWI ANAKHALA MUNTHU WOYAMBA KWAMBIRI KUTI ANAKHALA NDI MOYO.

KODI MUNTHU AMENEYU ANGAKHALE WABODZA?

KODI BUKU LIMENE LINAVUMBULISIDWA PAIYE LIDZAONEDWA KUTI ANALEMBA NDI IYE

## 9.) MAPETO

Mutu wa zipembedzo, womwe umawonedwa mwa ena, ndi umodzi womwe ndi wovuta kwambiri kuuchepetsa kukhala mawu ochepa. Pachifukwa ichi, tayesetsa momwe tingathere kuphatikizira mwachidule mwachidule zomwe tidawona kuti ndizofunikira kugawana.

Tikukhulupirira kuti tachita zimenezi mwaulemu, popanda mzimu wodzikuza pochita zimenezi. Lingaliro la moyo siliri mu kudzikundikira chuma, koma kupeza njira yowona. Tiyeni tonse titsogoleredwe kunjira imeneyo. Ameen.

Kwa amene adauziridwa ndi bukuli, ndipo akufuna kuvomereza Chisilamu, tikukulimbikitsani kuti mupite ku Mzikiti wapafupi ndi kwanuko (malo opembedzera achisilamu) kuti mukalankhule ndi Imam (mtsogoleri) wa mzikitiwo. Njira yovomerezera Chisilamu ndi njira yachidule, koma yomwe siyenera kukhazikitsidwa payokha, popanda chitsogozo cha Imam wodziwa bwino kudzera mu ndondomekoyi.

Tili ndi chidaliro kuti pafupifupi owerenga aliyense amadziwa mzikiti umodzi mdera lomwe amakhala, kapena Msilamu m'modzi yemwe angakutsogolereni ku mzikiti wa komweko mdera lanu.

Mukalephera mbali zonse ziwiri, imelo yathu imayikidwa pachikuto kuti muthandizidwe.

Kwa iwo amene amawerenga bukhuli pazifukwa zamaphunziro chabe, tikukulimbikitsani kuti muwerenge bukuli ndi malingaliro ena.

Werengani ndi cholinga chofuna, mosiyana ndi kuphunzira. Kwa amene akuwerenga bukuli ndi zolinga zachipongwe chabe, ndi kunyoza chipembedzocho popeza zikhulupiriro zomwe zimawoneka zosamveka m’maganizo a munthu, ndiye kwa inu, tikuti ALLAH (Mulungu) akuongoleni.

Ndipo pomaliza, kwa Asilamu amenewo, akhale Asilamu atsopano kapena Asilamu “akale” omwe akuwerenga kabukuka, Allah (Mulungu) atisunge panjira yowongoka ndikuti tikhale chiongoko kwa onse. Ameen.

**If you have any questions related to Islam, please do not hesitate to contact us via:**

**<u>WhatsApp:</u> +27 61 625 6070 (SOUTH AFRICA)**

**<u>EMAIL:</u> theabuzaydinstitute@gmail.com**

**What is Islam? (Chichewa Translation)**

Revised
July 2025

The Abu Zayd Institute

English translation proof read by: The Majlisul Ulama of South Africa

Chichewa Translation by: Hasimi Issah

Chichewa translation proof read by: Ali Issah

Cover page artwork: Y Areff

**Contact details**

Cell No: +27 61 625 6070 (South Africa)
Email: theabuzaydinstitute@gmail.com
Website: www.abuzayd.org.za